# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA, LA 2025-2026 M'BOMA LA MCHINJI

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 ikuyembekezereka kukhala ya pakatikati, yosakhudzidwa ndi La Nina kapena El Nino.


Boma la Mchinji likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena mlingo woposera wokhazikika.

## October 2025





M'mwezi wa October madera ambiri mu boma la Mchinji akuyembekezeka kudzakhala opanda mvula koma pali mwayi oti madera ena akhoza kudzalandira mvula yochepera 30mm yomwe ingadzabwere ndi mphepo yamkuntho komanso ziphaliwali.

## November 2025





Mvula yokhazikika kapena kapena yocheperako ikuyembekezeka m'madera ambiri mu bomali kupatula pa boma ndi **SC Mawere** komwe tikuyembekezera kugwa mvula yochulukirapo.
Chiopsezo cha mvula ya mphepo komanso ya ziphaliwali ndi chokwera mu mweziwu.
**mvula yokhazikika ikuyembekezeka kugwa kuyambila sabata lachitatu la mweziwu.**

## December 2025





Madera ambiri a mbali ya ku madzulo adzalandira mvula ya mlingo wa pakati pa 250-300mm pamene 200 mm ikuyembekezeka m'madela a ku mmawa kwa boma la Mchinji. mvulayi ndi mlingo okhazikika kapena kuposera apo.

## January 2026




Mvula yokhazikika kapena kuposera apo ya mlingo wapakati pa 250-300mm ikuyembekezeka kugwa m'madela ambiri a pakati komanso a ku m'mwera kwa bomali mu mwezi wa January 2026.
Madela ozungulira pa Boma akuyembekezeka kuzalandira mvula yoposera 300mm.
Ng'amba yofikila sabata limodzi ikuyembekezeka m'mweziwu.


## February 2026




Mvula yokhazikika kapena yocheperako ikuyembekezeka m'madela ambiri m'boma la Mchinji.
Madera ambiri akuyembekezeka kuzalandira mvula ya mlingo wa 150-200 mm.


Pali kuthekera kodzakhala ndi ng'amba ya masabata awiri.

## March 2026




Madera ambiri akuyembekezeka kuzalandira mvula ya mlingo okwanira 150-200mm omwe uli mlingo okhazikika kapena oposera apo.

## April 2026





Boma la Mchinji likuyembekezeka kuzalandira 50–100mm omwe ndi m'mlingo okhazikika kapena kuposera apo mlingo.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kufika ku mapeto mu sabata lachitatu la mwezi wa April.

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26. Boma la Mchinji likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo. Nyengo yonse ya dzinja ikhala ya masiku apakati pa 130 ndi 140.Pali kuthekera kokhala ndi ng'amba yosapitilila masiku asanu andi awili miyezi ya January ndi February 2026.

Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.

| MCHINJI | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 6.71 | 21.388 | 10.9 |
| NOV | 42.672 | 102.393 | 84.8 |
| DEC | 175.583 | 274.016 | 259.3 |
| JAN | 235.94 | 298.09 | 306 |
| FEB | 174.548 | 235.959 | 191.6 |
| MAR | 111.548 | 216.984 | 208.1 |
| APR | 33.456 | 82.897 | 41.4 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu mwezi wa December 2025**


Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zapangidwa ndi kusindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: